

NYA_TTB_1105_SCRIPT

1 Yohane : 4:1-3

Mutu : Wokhulupirira ayenera kuchenjera ndi aphunzitsi onyenga.

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero Ambuye atitsogolere ndi mau apa Miyambo 2:1-5, amene akuti, “Mwananga, ukalandira mau anga, ndi kusunga malamulo anga; kucherera makutu ako kunzeru, kulozetsa mtima wako kukuzindikira; ukaitanansoluntha, ndi kupfuulira kuti ukazindikire; ukaifunafuna ngati siliva, ndi kuipwaira ngati chuma chobisika; pompoudzazindikira kuopa Yehova ndi kumdziwadi Mulungu.”

Mupologalamu yatha tinali kusanthula 1 Yohane 3:17-4:1, pa nkhani yakuonetsedwakwa chikondi muntchito kuti ndicho chitsimikizo chakuti pemphero lidzamveka. Ndipo lero pa 1 Yohane 4:1-3, tiunika nkhani yakuti wokhulupirira ayenera kuchenjera ndi aphunzitsi onyenga.

1 Yohane 4

Tsopano talowa mugawo lobvuta la mau a Mulungu la buku la 1 Yohane chifukwa tiyamba kusanthula nkhani yokhudza mizimu, popeza palibe m'modzi yense wa ife amene akudziwa bwino. Chifukwa chachiwiri ndi chakuti ife wokhulupirira tiri kale m'dziko la mdierekezi. Ndifuna muone kuti nthawi yonse pamene atumiki alalikira mau a Mulungu, amene amatsutsana ndi m'dierekezi, pamakhala kachisokonezo kena kake. Kawiri-kawiri, pamisonkhanoyotere timaona kuti mdierekezi amadzetsachisokonezo ngakhale kudzera mwa ana, kusokosera ndi kumangoliralira. Kutanthauza kuti satana ali ndi njira zambiri zomwe amagwiritsa ntchito pofuna kusokoneza ntchito ya Mulungu.

Pachifukwa chimenechi, tikunenetsa kuti iyi ndi ndime ina yofunika kwambiri, koma pali ngozi yakuti pamene tizama kapena kuika chidwi chathu kwambiri pachiphunzitsa cha mdierekezi, moyo wathu umadzazidwa ndi ziphunzitsa zake ndi kumamuopa kwambirim'dierekeziyo. Ndikunena mau amenewa chifukwa palizipembedzo zina zomwe zinakhazikikapaziphunzitsa za satana,

kotero kuti zaiwala kudziwa zomwe Baibulolimaphunzitsa zokhudza satana.

Tsono m'ndime zisanu ndi imodzi, Mtumwi Yohane akuchenjeza kuti wokhulupirira ayenera kuchenjera ndi aphunzitsi onyenga.Chenjezoli likuperekedwaatangotsiriza kumene kukhazikitsa chiphunzitso chakuti ife wokhulupirira tinapatsidwa Mzimu wa Mulungu ndipo kuti tinapatsidwa kudzoza ndi kuzindikira zinthu za Mulungu.

1. Okonedwa, musamakhulupirira Mzimu uli wonse, koma yesani mizimu ngati ichokera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m'dziko lapansi.

Tsopano talowa m'chiphunzitso cha Mzimu, ndipo Baibulo likunena zinthu zambiri zokhudza mizimu.Mwachitsanzo pamene tiwerenga Ahebri 1:7, tipeza mau akuti, “Ndipo za angeloanenedi, amene ayesa angelo ake mizimu, ndi omtumikira Iye akhale lawilamoto.” Ndipo tikatsika pang'ono pa verse 14, tipeza mau akuti, “Kodi siiri yonse mizimu yotumikira, yotumidwa kuti itumikire iwo amene adzalowa chipulumutso?”

Tsono inesindinamuonepo mngelo, komanso asanayambewandionejera. Ndiye ndimakhulupirira kuti popeza mwa ine, muli Mzimu wa Mulungu, sipayeneranso kukhala kusintha kwina malinga ndi chikonzero chimenechi. Ndikunena mau amenewa chifukwa ndikuona kuti ndikoyenera kuti ndidalire kwambiri Mzimu Woyera kusiyana ndi mngelo amene ndi wolengedwa. Kutanthauza kuti inu ndi ine, tiyenera kudalira kwambiri pakudzazidwa ndi Mzimu Woyera mumtima mwathu ndi m'moyo mwathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunena kuti alipo angelo abwino, amene amatumikira Mulungu komanso pali angelo amene anaukira Mulungu. Tsono angelo awa, m'mau a Mulungu amatchedwa mizimu. Mukumbukira kuti m'nthawi ya Ambuye Yesu, munalikutchulidwa mizimu yoipa. Iyi ndimizimu yomwe ikutchulidwa kuti ndi ziwanda (demons) monga momwe mau a Mulungu anenera.

Ndiye ife wokhulupirira tikuchenjezedwa kwambiri kuti tiyenera kubvaladi zida zonse za Mulungu popeza tiri m'nkhondo yaikulu ya mzimu, yomwe ndiyoposa mphamvu yathupi. Tamvani Paulo pa

Aefeso 6:12, akunena kuti, “Chifukwa kulimbana kwathu sitilimbana nawo mwazi ndi thupi, komatu nawo maukulu ndi maulamuliro ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno ndi a uzimu a choipa m’zakumwamba.” Tere mukhoza kuona kuti ndime iyi, ndiyomwe ikuonetsa chithunzi chakuti satana anakonzekera bwino nkhondoyipakugwiritsa ntchito ziwanda. Tsono munkhondo imeneyi, tikuona kuti satana anaika magulu-magulu a ziwanda; zina ndi zamphamvu kwambiri kuposa zina kufikira zing’onozing’ono.

Ndiye Mtumwi Yohane akunena kuti, “Okondedwa, musamakhulupirira Mzimu uli wonse.” Pano ndifuna kunena mosabisa kanthu kuti mphamvu ya Mulungu ikunyozeka poyera maka-maka pakati pa anthu ophunzira, ndipo kuti satana akupembedzedwa poyera. Kutanthauza kuti ilipo mipingoyopembedza satana m’dziko lathuli. Ndipo ngozi zambiri zikuchitikazi komanso umbanda wochulukira ukuchitikawu, ndichifukwa chakuti afuna kukondweretsa satana. Tikunena kuti ngati anthu afikapomasaka anthu anzawo ngati gwape, monga kupha anthu achiAlbino, akazi, amuna, ana ngakhalenso iwoamene

ali ndi madazi. Zonsezi zikungoonetsakukulakwa mphamvu ya satana momwe akugwiritsa ntchito ziwandazosiyana-siyana.

Taonani ziwanda zina zikugwiritsidwa ntchito ngakhalenso m'mabuku monga buku lotchedwa "Jonathan Livingston Seagull" lolembedwa ndi Richard Bach. Mkulu uyu, adanena kuti adalemba bukuli osati ndi mau ake, koma amachita kuuzidwa mau ndipo iye anali kulemba. M'buku limeneli muli mbiri ya mau a Mulungu koma yokhudza mbalameyaing'ono ya m'nyanja yomwe ili ndi makhalidwe a munthu. Mkulu uyu, akunena kuti anaulukanafika kumalo kwina komwe kulibe choipa chilichonse ndipo kuti chilengedwe cha munthu chinachitika ndi chimbalame ya m'nyanja. Buku limeneli limaphunzitsa kuti kulibe tchimo, kulibe matenda komanso kulibe imfa, kotero kuti zinthu zonsezi ndizopeka. Ndipo zinthu zomwe Baibulolimaphunzitsa kuti ndi tchimo, ndizo zinthu zabwino monga ufulu ndi kuchita zinthu zonse monga munthu afuna. Anzanga, ndifuna muone kuti zinthu izi, sizatsopano ayi, koma zikuchokerakugahena. Kutsimikiza kuti ichi, ndicho chipembedzo cheni-cheni cha satana. Kodi zinthu izi, mulibe kapena siziphunzitsidwa m'dziko lathuli?

Masiku ano mphamvu ya ziwanda ikuonetsedwa kwambiri m'nyengo iyi, momwe maganizo a munthu akhazikikapakukundika chuma cha panso pano. Mtima uwu, ndiwo umene ukuchotsa munthu pakuika maso ake pa Mulungu ndi kuika maso ake pa chuma. Tikunena kuti lero lino munthu wanzeru ngakhale m'masukulu athu, ndiye amene salabadira mau a Mulungu. Kutanthauza kuti munthu wina aliyense amene akangamira mau a Mulungu, saoneka wanzeru mpang'onopomwe. Pachifukwa chimenechi, tikuona kuti achinyamata athu ambiri achokadi pamau a Mulungu, chifukwa sakulandira chiphunzitsa cha m'Baibulo.

Tsono Mtumwi Yohane wangotsiriza kumene kuphunzitsa wokhulupirira onse kuti ayenera kukondana ndi kuthandizana wina ndi mnzake, koma pano akunena kuti tiyenera kuchenjera. Paulo adalembera Afilipi 1:9, amene adawakonda kwambiri ndipo adati, "Ndipo ichi ndipempha, kuti chikondi chanu chisefukirechionjezere, m'chidziwitso, ndi kuzindikira konse." Nkhani iyi, ikuti ndichinthu chabwino kwambiri kukondana, koma tiyenera kudziwa kuti tiri m'dziko loipa. Ili, ndidziko lomwe

lidzatinnyenga kotero kuti tiyenera kuchenjeza nalo. Tikunena kuti liwulachikondilikugwiritsidwa ntchito moipa ndi satana, kusiyana ndi momwe Mulungu aphunzitsira. Tere ndichifukwa chake Paulo anali kuwapempherera akristu aku Filipi kuti achuluke m'chikondi ndi kukhala ndi chidziwitso choyenera. Kunena kuti iwo samayenera kulandira chilichonse chomwe chikuchokera kwa munthu amene akudzitchula kuti ndimkristu, popeza ambiri a iwowa, sakristu konse. Tikunena kuti anthu ambiri, makamakaachinyamataalowa m'chipembedzo cha satana m'dzina la chikondi. Ichi, ndichimene Paulo analikupempherera akristu aku Filipi kuti sayenera kungokula m'moyo wachikondi wokha, komanso ayenera kukulam'chidziwitso cha momwe zinthu zikuyendera. Kutanthauza kuti inu muyenera kuona liwu la chikondi mosamalitsa chifukwa liwu limeneli lalowetsa anthu ambiri m'chipembedzo cha satana.

Yohane akuchenjeza kuti inu ndi ine, sitienera kukhulupirira Mzimu uliwonse, koma tiyese mizimu. Tikunena kuti pamene inu mukumva kuti mtumiki wina ali ndi mphamvu ya Mulungu yopereka machilitso, kapena chuma, simuyenerakungotengeka

popanda kuyesa Mzimu womwe akugwiritsa ntchito. Ndikunenetsa pano kuti alipo anthu amene akudzitchula kuti akutumikira Mulungu, koma ndiwonyenga kotero akubisalirakudzina la Kristu.

Ndiye Yohane akunenetsa kuti, “Aneneri onyenga ambiri aturuka kulowa m’dziko lapansi.”Tsono Paulo pa 1 Akorinto 14:3, anagwiritsanso ntchito liwu lomweli la “aneneri onyenga kuti ndiwo aphunzitsi onyenga.”Tamvani akunena kuti, “Koma iye wakunenera alankhula ndi anthu chomangirira ndi cholimbikitsa ndi chosangalatsa.”Kutanthauza kuti kunenera kuyenera kukhala kophunzitsa (chomangirira), cholimbikitsa ndi chosangalatsa.

Wokondedwa anzanga apaulendo, lero liwu la kuneneralikugwiritsidwa ntchito mosayeneramosemphana ndi momwe mau a Mulungu anena.Ichi, ndichimene Mtumwi Yohane akunena kuti inu ndi ine, ngati wokhulupirira tiyenera kuchenjera osakonda atumiki onse ngakhale adze m’dzina la Ambuye.Awa, ndiwo anthu oopsa kwambiri kusiyana ndi njoka yomwe iliramuudzu.Tikunena kuti munthu uyu, ndiye woopsa kwambiri chifukwa akhoza kutenga Baibulo ndi kumaphunzitsazabodza.

2. M'menemo muzindikira Mzimu wa Mulungu: Mzimu uli wonse umene ubvomereza kuti Yesu Kristu anadza m'thupi, uchokera mwa Mulungu.

Pano Mtumwi Yohane akunena kuti ife tikhoza kuzindikira Mzimu wa Mulungu pamene Mzimuyoabvomereza kuti Yesu Kristu anadza m'thupi. Kunena kuti chinthu choyambirira kuzindikira ndi Mzimu woona ndi kuzindikira kuti Kristu anabadwira m'Betelehemu. Nkhani ikuti Yesu Kristu anabadwira mu Betelehemu, kunena kuti Mulungu anadzitsitsa ndi kubvala thupi lamunthu. Apa, ndipo pamene mtumiki wina aliyense woona, ayenera kuyambira chiphunzitso chake. Ndikunena mau onsewa chifukwa kungokhazikika pa kufa ndi kuikidwa m'mandakwa Yesu Kristu, sizipereka tanthauzo leni-leni la kukhala Mpulumutsi pokha-pokha timzindikire kuti ndiye Mulungu komanso munthu. Ndikunena kuti chizindikiro chimodzi chakuti inu mukhoza kuzindikira aphunzitsi onyenga, ndichakuti iwowa sabvomereza kuti Kristu ndi Mulungu ndithu. Apa, tikunena kuti aneneri onyengawa amalankhulabezokometsera ndi zabwino za Ambuye Yesu. Taonani kuti aneneri otere,

amakambazodabwitsazaumwana wake ndi kuti Yesu anali mwana wodabwitsa m'dziko lonse. Aneneri amenewa amanena kuti Yesu anali kukonda chipembedzo kotero kuti amakhaladi mwa Mulungu, osati kuti ndiye Mulungu amene ayi. M'malo make aphunzitsi onyengawa amanena kuti Yesu Kristu anali ndi chidziwitso chachikulu chokhudza Mulungu kusiyana ndi munthu wina aliyense. Iwowa amanena kuti palibe munthu wina womposa Kristu. Mwanjira ina aneneri onyengawa amanena zokoma zambiri za Yesu Kristu, koma sanganene kuti ndiye Mulungu, amene anaonetsedwa m'thupi ayi. Tsono Yohane akunena za dzina lakuti "Mau" mu Uthenga Wabwino. Iye akunena kuti Kristu ndiye "Mau," amene anali ndi Mulungu pachiyambi, amene analenga zinthu zonse komanso amene anakhala munthu. Kutsimikiza nkhani yakubadwakwa Yesu Kristu ku Betlehemu. Ndiye tikunena kuti pamene inu mukana umulungu wa Kristu ndi umunthu wake zikutanthauza kuti mukukananso ntchito yomwe Kristu anagwira mwa imfa yake ya pamtanda popeza ntchito yonseyi inachitika chifukwa chakukhala Mulungu komanso munthu. Tsono chimene aneneri onyengawa amachita ndiko kumkometsa Kristu mopitilira muyeso ndi cholinga chakuti inu musaone kuti akumutsitsapokana

umulungu ndi umunthu wake. Tere lero, ndifuna inu mutchere makutu anu kuchiphunzitsa chimenechi ndipo muyenera kudziwa kuti Kristu ndiye chimene akunena kuti ali. Tamvani Kristu mwini pa Yohane 14:9-10 akuchitira umboni mau amenewa pamene akuti, “Iye amene wandiona Ine waona Atate; unena iwe bwanji, mutionetsere Atate? Sukhulupirira kodi kuti ndiri Ine mwa Atate, ndi Atate ali mwa Ine? Mau amene ndinena Ine kwa inu sindilankhula kwa Ine ndekha; koma Atate wokhala mwa Ine achita ntchito zake.”

Yohane mundime iyi, akutsutsiratu chiphunzitsa chonyenga chomwe chimanena kuti Kristu anadza pamene Yesu pakubatizidwa ndipo kuti anachoka pamene anapachikidwa pamtanda. Ichi, sichimene mau a Mulungu amaphunzitsa ayi. Taonani mau a Mulungu amaphunzitsa kuti mwana amene anabadwa mu Betlehemu sadali mwana wodziwika bwino chabe, imfa yake yapa mtandasinali imfa wamba, ndipo kuti pamene anauka kwa akufa, anauka ndi thupi lake lomwe. Ndipo Paulo pa Aroma 4:25, akunena kuti, “Amene anaperekedwa chifukwa cha zolakwa zathu, naukitsidwa chifukwa cha kutiyesa ife olungama.”

Komanso Yesaya 9:6, akunena kuti, “Pakuti kwa ife mwana wakhandawabadwa, kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa.” Kutanthauza kuti mwana anabadwa monga munthu, koma mwana wamwamuna anapatsidwa kwa ife. Apa, akunena kuti Mwana wa mwamuna anachokera kosayamba, m’masiku akale, koma mwana muumunthu wake ndiye anabadwa kudzera mwa namwali. Kutsimikiza kuti Yesu Kristu ndiye woposa mwana, woposa ana onse padziko lapansi monga akunena aneneri onama. Iyeyu ndiye Mfumu ya mafumu ndi Mfumu ya mtendere m’dziko lotopetsa lomwe tikukhalamoli. Ndiye tikunena kuti ichi, ndicho chizindikiro chimodzi cha momwe mungamdziwire mneneri wonyenga.

3. Ndipo Mzimu uli wonse umene subvomereza Yesu suchokerakwa Mulungu; ndipo uwu ndiwo Mzimu wa wokana Kristu umene mudamva kuti ukudza; ndipo ulimo m’dziko lapansi tsopano lomwe.

Nkhani ili mundime ino, ikuti wokana Kristu akubwera. Ndiye m’mbuyomu tidanena kuti inu mukhoza kumukana Kristu munjira ziwiri; poyamba mukhoza kukana Atate ndi Mwana ndipo pamene muyeseza kukhala Kristu ndiye kuti muli kumukananso. Pamene

tiwerenga Chibvumbulutso 13, tipezamo zirombo ziwiri. Chirombo choyamba ndicho wokana Kristu, amene ndi wolamulira dziko lonse wamphamvu, amene adzalamulira dziko lonse ndi mphamvu zake. Ndiye palinso wolamulira wamphamvu wachipembedzo, amene ali mneneri wonama. Uyu, ndiye adzalimbikitsa dziko lonse kulambira chirombo choyamba chija. Chirombochachiwirichi, chidzabwera monga nkhusa, pamene chili chimbalangondo, koma chidzatsaza Kristu. Apa, ndipo pamene ndikukhulupirira kuti awa, ndianthu awiri, amene adzakwaniritsa chomwe mau a Mulungu anena.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikunena kuti mukaonetsetsa zomwe zikuchitika m'dzikoli, mupeza kuti pali chikonzero chakuti pakhale wolamulira dziko m'modzi ndimkuluwachipembedzom'modzi. Mtsogoleri uyu, ndiye amene adzayesakudzetsa mtendere m'dziko lonse mwakanthawi kochepe, koma ndiyo idzakhala nthawi yoopsya kwambiri m'dziko lapansi.

Tsono pamene tiwerenga 1 Yohane 2:18, tipeza mau akuti, "Ndipo monga mudamva kuti wokana Kristu akudza, ngakhale tsopano alipo okana Kristu ambiri; mwa ichi tizindikira kuti ndi nthawi yotsirizaiyi." Awa, ndiwo aneneri onyenga amene achulukana pakali

ano. Koma tiyenera kudziwa kuti ndiwo amene akusendeza nthawi kufika kuchimalizirokwa nthawi yapansi pano. Tsono pamene Yohane akunena kuti ife wokhulupirira tiyenera kukonda anzathu, sakunena aphunzitsi onyengawa koma akristu wona. Tere ndichifukwa chake Yohane watenga nthawi yaikulu yoterekutichenjezaza aneneri onyenga kuti adzakana umunthu wa Kristu. Kutsindika kuti kubadwa kwa Ambuye Yesu kudzera mwa namwali ndikofunika kwambiri.

Tiyeni titsirize ndi funso lakuti, kodi ndizotheka munthu kukhala mkristu weni-weni pamene sabvomereza kuti Kristu anabadwa kudzera mwa namwali? Yankho likuti ndizosatheka chifukwa kukana kubadwa kwa Kristu mwa namwali, ndicho chizindikiro cha mphunzitsi wonyenga. Nkhani ikuti inu mukhoza kuononga chikhulupiriro cha chikristu mwanjira yokana imfa ya Kristu pamtanda chifukwa cha machimo athu komanso ndi kuuka kwa akufa ndi thupi lake lomwe. Tere ndichifukwa chake Yohane akunena kuti inu ndi ine, sitienera kunyengedwa ndi aneneri wonama ayi.

Kwalerotilekeza pano. Koma tinali kusanthula 1 Yohane 4:1-3,
momwe timaunika nkhani yakuti wokhulupirira ayenera
kuchenjera ndi aphunzitsi onyenga.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!